



NAMBIRO ZONE EXAMINATION BOARD

2023 STANDARD 8 MOCK EXAMINATIONS

CHICHEWA

(100 Marks)

Subject Number: P025

Time allowed: 2 hours 15mins

09:00 – 11:15 am

NAME: (Surname First) _____

SCHOOL _____ DATE _____

- 1. Onetsansi kuti pepala ili lili ndi masamba asanu ndi limodzi (6).**

- 2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: Gavo A, B, C ndi D.**

- 3. Lembani dzina lanu ndi nambala yanu ya mayeso pamwamba pa tsamba lino.**

- 4. Lembani chimangirizo kapena kalata mu Gavo A ndipo muyankhe mafunso onse mu Gavo B, C ndi D.**

Lembani yankho la mu **Gavo A** pa pepala lomwe lili kumathero kwa mafunso a mu gawoli.

- 5. Yankhani mafunso a mu Gavo B ndi C m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse.**

- 6. Yankhani mafunso a mu Gavo D pozunguliza lembo lokhoza pafunso lililonse.**

- 7. Muchitebulo chilli pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lilikutsogolo kwake.**

- 8. Perekani kwa oyang'anira kulemba mayeso (imvijireta) pepala lonseli nthawi ikakwana.**

Funso	Chongani zomwe mwayankha	Muno musalembemo
1		
2		
3		
4		
5		
6 - 10		
11 - 15		
16 - 20		
21 - 25		
26 - 30		
31 - 33		
34- 35		
36 - 40		
41 - 45		

GAWO A (MALIKISI 30)

LANGIZO: Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali mmunsiwa:

Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu:
 ‘CHITUKUKO CHA M’DERA LATHU’. Mwazina tsatani izi polemba:

Ndime yovamba:

- Chitukuko chomwe chikuchitika m’dera lanu
- Tsiku lomwe chitukuko chidayamba
- Midzi yomwe yatenga nawo mbali pachitukuko

Ndime yachiwiri:

- Momwe mungasamalire chitukuko
- Momwe mungalimbikitsire anthu kuti chitukukochi chiwapindulire
- Phindu lomwe mukupeza kuchokera kuchitukukochi

Ndime yachitatu:

- Zomwe mukuchita kuti chitukuko chipite patsogolo

Kapena

2. Lembani kalata kwa mzanu yomufotokozenza za katundu yemwe mwaberewa myumba mwanu. Mwazina tsatani izi polemba:

Ndime yoyamba

- Cholinga cha kalata
- Katundu yemwe wabedwa
- Nthawi yomwe katundu wabedwa

Ndime yachiwiri:

- Munthu yemwe mukumuganizira za kubedwa kwa katundu.
- Zomwe mukuchita kuti katundu apezeke
- Anthu omwe akukuthandizani kuti katundu apezeke

Ndime yachitatu

- Mwachita chiyani ndi munthu yemwe mukuganizira kuti waba katundu

GAWO B (MALIKISI 20)
KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi kenako muyankhe mafunso otsatirawo.

Chakudya ndi chofunika kwambiri kwa munthu, nyama ngakhalenso zomera. Popanda chakudya anthu, nyama ndi zomera zimafa. Kupeza chakudya sintchito yophweka ayi. Nkofunika kusamalira zakudya tikazipeza. Enanso sasamala zakudya amangotaya makombo monga mkute ndi ndiwo. Kutero ndikuononga.

Pali njira zosiyansiyana zosamalira zakudya. Njirazi zimasiyanasiyana malingana ndimitundu ya zakudya. Mwachitsanzo, chimanga chachiwisi ena amati dowe, kapena mondokwa wophika tikhoza kuwusamalira powupanga mfodo. Chimanga chouma tikhoza kuchisamala pochithira mankhwala monga amene amachiteteza kwa ankafumbwe. Tikamaphika nsima tiyenera kukhala ndi mulingo woyenera wa madzi molingana ndi kukula kwa banja lathu. Mkute tiziwsungunula ndikuuphikanso tsiku lotsatira lake osati kumangotaya.

Ndiwo zamasamba monga nkhwani, mtambe, khwanya, limanda, luni ndi bowa zilinso ndi njira zake zozisamalira. Ena akapeza ndiwo zambiri zotere amazisunga mzikwatu. Mzikwatuzi ndiwo zimasungidwa nthawi yayitali. Zikhoza kutha chaka osaonongeka ngati zikwatuzo zili pa malo opanda chinyezi. Ndiwozi siziwola chifukwa zimakhala ndi mchere. Mfutso umathandiza mnyengo ya mwamvu pamene ndiwo zamasamba zauma mminda, mmadambo komanso mnkhalango. Mfutso wa mtambe wophatikiza ndi mphalabungu ndi ndiwo zokoma kwambiri.

Yankhani mafunso otsatirawa:

- a. N'chifukwa chiyani chakudya ndi chofunika kwambiri? (malikisi 2)
-
- b. N'chifukwa chiyani tiyenera kusamalira chakudya tikachipeza? (malikisi 2)
-
- c. Tchulani njira imodzi yomwe anthu amaonetsa powononga zakudya. (malikisi 1)
-
- d. Tchulani mdani wa chimanga chouma. (malikisi 1)

- e. Perekani mawu omwe akufanana ndi awa munkhaniyi:
 i. nsima yotsala (malikisi 1)
- ii. ndiwo zoumitsa (malikisi 1)
- f. Nchifukwa chiyani njira zosamalira zakudya ndi zosiyana? (malikisi 2)
- g. Perekani mitundu itatu ya ndiwo zamasamba. (malikisi 3)
- i. _____ ii. _____
 iii. _____
- h. Tchulani ntchito ya chikwatu. (malikisi 1)
- i. Chomwe chimapangitsa ndiwo kuti zisawole ndi chiyani? (malikisi 1)
- j. Ndi ndiwo ziti zomwe zili zokoma kwambiri? (malikisi 1)
- ii. Tchulani mdani wa zikwatu. (malikisi 1)
- k. Perekani mutu wa nkhaniyi (malikisi 2)

GAWO C (MALIKISI 10)

Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli
 Werengani kankhanika ndipo muyanke mafunso
 otsariwo.

Anasuweti: Odi!

Achakwana: Eee! Fikani konkuno. Kodi kwagwanji
 usiku uno?

Anasuweti: Kunyumbaku Sikuli bwino, a phwanu
 ndi amene adwala.

Mafunso.

a. i. Ndi malonje anji amenewa?

_____ (malikisi 1)

ii. Malonjewa akuchitikira kuti?

_____ (malikisi 1)

iii. Mau oti mphwanu akutanthauzanji?

_____ (malikisi 1)

b. Kodi oyenda pansi ayenera kuyenda mbali iti
 yamsewu?

_____ (malikisi 1)

c. Perekani njira imodzi imene mungasamalire
 pakhomo panu.

_____ (malikisi 1)

5. pangani ziganizo ndi mawu awa: (malikisi 5)

a. ndi

_____ (malikisi 1)

b. patali

_____ (malikisi 1)

c. wakuda

_____ (malikisi 1)

d. chilengedwe

_____ (malikisi 1)

e. mpaka

(malikisi 1)**GAWO D (40 MALIKISI)**

Mafunso 6 mpaka 10: Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekeda mzere kensi kwavo m'ziganizo zotsatirazi.

6. Pakuti sindinamuonepo, sindimudziwa.

- | | |
|--------------|-------------|
| A. mfotokozi | B. muonjezi |
| C. mlumikizi | D. dzina |

7. Iye amayenda mothimbwidzika.

- | | |
|--------------|-------------|
| A. mperekezi | B. mnemi |
| C. dzina | D. muonjezi |

8. Pali chidani chachikulu pakati pa Maria ndi Rute.

- | | |
|------------|---------------|
| A. dzina | B. mlowammalo |
| C. mvekero | D. mfotokozi |

9. Masewero omwe anawo amasewera ndi mpira.

- | | |
|--------------|---------------|
| A. mfuwuliro | B. mnemi |
| C. mfotokozi | D. mlowammalo |

10. A Phiri adaba chiyani?

- | | |
|-------------|---------------|
| A. dzina | B. mlowammalo |
| C. muonjezi | D. mlumikizi |

Mafunso 11 mpaka 15 Tchulani mitundu ya msintho wa aneni omwe ali ndi mzere kensi kwavo m'ziganizo zotsatirazi.

11. Kalatayi yalembeka bwino.

- | | |
|--------------------------|-----------------------|
| A. wonyazitsa | B. womchitira |
| C. wochitidwa mchibisira | D. wochitidwa poyeria |

12. Iwo ankapenyetsetsa pamene ndinkabwera.

- | | |
|-----------------------|---------------------|
| A. wochititsa | B. wochititsitsa |
| C. wochitidwa poyeria | D. wobwerezabwereza |

13. Pakali pano ndikusinkhasinkha choti ndichite.

- | | |
|---------------------------|-----------------------|
| A. wobwerezabwereza | B. wochititsa |
| C. wochitidwa m'chibisira | D. wochitidwa poyeria |

14. Mwana wamenyedwa.

- | | |
|-----------------------|------------------|
| A. wochitidwa poyeria | B. wochititsa |
| C. wonyazitsa | D. wochititsitsa |

15. Anthuwa amakambiranana nkhani zoseketsa zedi.

- | | |
|---------------------------|----------------|
| A. wochitidwa m'chibisira | B. wochitirana |
| C. wobwerezabwereza | D. wochititsa |

Mafunso 16 mpaka 19 Sankhani ntchito za mayina omwe atsekeda mzere kensi kwavo m'ziganizo zotsatirazi.

16. Yohane wapita kumsika.

- | |
|-----------------------------------|
| A. kukhala pamtherankhani |
| B. kukhala dzina |
| C. kukhala dzina lolandira kanthu |
| D. kukhala mwininkhani |

17. Ndipita kuchipatala ndi mwana.

- | |
|--|
| A. kukhala pamtherankhani wa mperekezi |
| B. kukhala mtsirizo wa mnemi |
| C. kukhala mwininkhani |
| D. kukhala mlowammalo |

18. Patsala paja pagona chinziri.

- | | |
|----------------|-------------------|
| A. mwininkhani | B. pamtherankhani |
| C. msonyamalo | D. dzina lapadera |

19. Njoka yagwira chule.

- | |
|-----------------------------|
| A. dzina lolandirira kanthu |
| B. pamtherankhani |
| C. dzina lapadera |
| D. mwininkhani |

Mafunso 20 mpaka 23: Sankhani ntchito za 'ndi' zomwe zatsekeda mzere kensi kwavo m'ziganizo zotsatirazi.

20. Iye ndi mnzanga

- | | |
|----------------------|----------------------|
| A. kukhla mnemi | B. kukhala mlumikizi |
| C. kukhala mperekezi | D. kukhala mvekero |

21. Ndabwera ndi mchemwali wanga.

- | | |
|--------------|--------------|
| A. mlumikizi | B. mperekezi |
| C. mvekero | D. mnemi |

22. Amayi ndi abambo akudyera limodzi.

- | | |
|--------------|--------------|
| A. mnemi | B. mperekezi |
| C. mlumikizi | D. mvekero |

23. Mumange mtolovo kuti ndi.

- | | |
|------------|------------------|
| A. mvekero | B. mgwirizanitsi |
| C. mnemi | D. mlumikizi |

Mafunso 24 mpaka 26: Sankhani chachikulu ndi chaching'ono cha mawu omwe atsekeda mzere kensi kwavo m'ziganizo zotsatirazi.

24. Galu woyeria uja waphedwa.

- | | |
|------------|------------|
| A. kamuna | B. msona |
| C. chiunda | D. mphonda |

25. Bambo ake adabwera ataledzera.

- A. mbululu B. khanda
 C. mnyamata D. msona

26. Ng'ombe zonse zabedwa.

- A. kang'ombe B. msona
 C. mkulumutu D. mbande

27. M'madzimo mwangwera chule.

- A. chiunda B. msona
 C. mbululu D. kachule

Mafunso 28 mpaka 31 Sankhani matanthauzo a zining'a zomwe zatsekeda mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatirazi.

28. Pamene timafika kumsika tinapeza dothi la anthu

- A. kuchepa kwa anthu
 B. kupakidwa matope
 C. kukhala pansi
 D. kuchuluka kwa anthu

29. Iye anabisala pachipande pamene amafunsidwa kuti ayankhe mlandu.

- A. kuthawa B. kuzemba
 C. kunama D. kubisala

30. Tinalephera kugona tulo chifukwa tinagona pa lumbe

- A. kugona pakconde B. kugona osafunda
 C. kugona pansi D. kugona ndi njala

31. Musamakonde kuyenda ndi kanga ndi wamba.

- A. munthu waukali
 B. munthu wamwano
 C. munthu waulesi
 D. munthu womana

Mafunso 32 mpaka 35 Sankhani mawu amene akupereka matanthauzo a zilapi zotsatirazi.

32. Alira atadzimanya yekha.

- A. nkhululu B. nungu
 C. mbalame D. tambala

33. Mfuti yanga yolasira kumbuyo.

- A. zombe B. mavu
 C. nkhululu D. chisoni

34. Walira opanda matumbo.

- A. ng'oma B. mbale
 C. mtondo D. kamwa

35. Bwenzi usiku okha.

- A. mnzako B. chovala
 C. chofunda D. chakudya

Mafunso 36 mpaka 38. Sankhani mitundu ya nthambi ya chiganizo yomwe yatsekeda mzere kunsi kwake.

36. Kumudzi komwe ndidabadwira ndi kuno.

- A. ya dzina B. ya muonjezi
 C. yoyima payokha D. yamfotokozi

37. Sadaulule zomwe adagwirizana.

- A. yoyima payokha B. yadzina
 C. yamfotokozi D. muonjezi

38. Chinkana mulire, sindikuthandizani.

- A. ya muonjezi B. ya dzina
 C. yoyima payokha D. ya mfotokozi

Mafunso 39 mpaka 42: Sankhani mitundu ya mifuwu omwe atsekeda mzere kunsi kwavo m'ziganizo zotsatirazi.

39. Mayo! Ndi kufa ine.

- A. wodandaula B. wodabwa
 C. wokondwa D. wokalipa

40. Haa! Amuna anga akomoka.

- A. wodabwa B. wachisoni
 C. wolira D. wokondwa

41. Asa! Bwanji wandiponda chala?

- A. wokondwa B. wachisoni
 C. wokalipa D. kudandaula

42. Hehede! Musatero anzanga.

- A. wolira B. wachisoni
 C. wokalipa D. wokondwa

Mafunso 43 mpaka 45: Sankhani mawu ofanana m'matanthauzo ndi omwe atsekeda mzere kunsi kwavo mziganizo zotsatirazi.

43. Iye wagula chifuyo.

- A. bakha B. mbalame
 C. chiweto D. kakowa

44. Chikondi ali ndi batani.

- A. bitoni B. butawo
 C. balaula D. chipumphu

45. Chitopa ndi choopsa.

- A. dzoye B. imfa
 C. zaye D. utilili